A CATECHISM,

NDIYO KUNENA,

MAYELUZO AKADAJIYELUZA MWENE WAKE ALI YENCHE, PACHOGOLO PA KUTENGEDWA KULIMBICHIDWA NI ASKOF.

Funcho.

Jina lako yani?

Yanko. N. or M.

Funcho. Yani adakuninka Jina ili?

Yanko. Achatate ndi achamaye wa pa Ubatizo yapo nidabatizwa; mmwemo nidachitidwa chiwalo cha Kristo, mwana wa Mlungu, ni wakuloa chokolo cha ufumu wa Kumwamba.

Funcho. Pamwepaja Achatate wanu ndi achamanu wa pa Ubatizo wadakuchitilani chiani?

Yanko. Wadalanga ni kulumbila vintu vitatu pa jina langa. Poyamba, kuti nimkane diabolo ni nchito zake zonche, vinyao ni va chaje va jiko lino loipa, ni kukumbila konche kwene zambi mnyama. Pa chiwili, kuti nivomele vonche vija va Mvano wao wa Kristo. Ni pa chitatu, kuti nivisunge ivo va pa voka vakumkondwecha Mlungu, ni matauko yake, ndi kuyenda yenda mmwemo masiku yonche ya kulama kwanga.

Funcho. Kodi wosaona kuti myeneledwa kuvomela ndi kuchita umo yawo wakuchitila chilanga?

Yanko. Etu zene; ndi Mlungu akanitangatila, sinichite chimwechi. Ndi ndimyamika Atate watu wa Kumwamba, pakuti ananitana niloe pa makalidwe aya ya kupulumuchidwa, mkati mwa Yesu Kristo Mpulumuchi watu. Ndi nimpempa Mlungu kuni-

pacha neema yake, nikaliletu mmwemo mpaka kutela kulama kwanga.

Catechist.

Fotokoza vija volunjana va Mvano wako.

Yanko.

Ndimvomela Mlungu Atate, Mwene mpavu zonche, Wopanga Kumwamba ndi jiko:

Ndi Yesu Kristo Mwana wake yeka yeka, Ambuye watu, Uyo adatengedwa mimba ndi Mzimu Woyela, Wobadwa ndi Maryamu *Virgin*, Wosauchidwa pa nyengo za Pontio Pilato, Wotalamichidwa pa msalaba, wakufa, woikidwa pa manda, Adachika pa malo pa mizimu; Siku la katatu adazyuka pa wakufa, Adakwela Kumwamba, Ndi akala panchi pa janja la kwene la Mlungu Atate mwene mpavu zonche; Kuchoka kumweko saaje kuwalamula wakulama ndi wakufa.

Ndimvomela Mzimu Woyela; Church Loyela ndi Katoliko; Kusanganizana kwa Woyela; Kulekeledwa zambi; Kuzyuka kwa tupi; Ndi Kulama kwa vyaka. Amen.

Funcho. Ujiyeluza chiani maka maka pa vija va Mvano wako?

Yanko. Pakuyamba, ndijiyeluza kuvomela pa Mlungu Atate, Uyu wanipanga ine, ni jiko lonche.

Pa chiwili, pa Mlungu Mwana, Uyu waniombola ine, ni wana wa adam wonche.

Pa chitatu, pa Mlungu Mzimu Woyela, Uyo aniyelecha ine, ni kamu lonche losankidwa la Mlungu.

Funcho.

Udanena, kuti Achatate ni Amanu wa pa Ubatizo wadakuchitila chilanga, kuti ukadasunga matauko yake Mlungu. Unifotokozele yalipo yangati?

Yanko. Kumi.

Funcho. Ndi yati?

Yanko.

Yamweyaja Mlungu adanena pa Chapter ya makumi yawili ya Exodus, kuti, Ine Ambuye Mlungu wako, Uyo adakutulucha pa jiko la Egupto, pa nyumba ya ukapolo.

I. Usakala ndi achimlungu wena pachogolo pa ine.

II. Usajipangila chintu chosepa, ingakale chintu chofwanana ndi chili chonche cha kumitambo kumwamba, pena cha pa jiko panchi, pena cha pa maji panchi pa jiko. Usavilambila, usavipotela: chifuko Ine Ambuye Mlungu wako ndili Mlungu mwene nchanje, ndibwezela voipa va achatate pa wana wao, ni pa vijukulu vao ni pa wana wa vijukulu vao kwa yawo wakuniipila, ndi kulangiza ubale kwa maelf kwa yawo wanikondawo, ndi wakusunga matauko yanga.

III. Usachula chaje Jina la Ambuye Mlungu wako: pakuti Ambuye sangamchite wopanda mlandu achulayo chaje Jina lake.

IV. Ulikumbukile siku la kupuma, ndi kuliika pa loka. Ujipota nchito masiku yasano ni limoji, ni kuchita votumikila vako vonche; siku la kasano ni kawili ndilo siku la kupuma la Ambuye Mlungu wako. Usachita votumikila vili vonche, iwe, ni mwana wako mwamuna, ndi wamkazi, ni wopotela wako, ni mbumba yako, ni ng'ombe zako, ni mlendo wa pa makomo yako. Pakuti pa masiku yasano ni limoji Ambuye adachita Kumwamba ndi jiko, nyanja, ndi vonche ivo vili mmwemo, ndi adapuma siku la kasano ni kawili; chimwechi Ambuye adalininka mwawi siku la kupuma, ndi kuliika pa loka.

V. Lemekeza atate wako ni amako; masiku yako yakale yanyinji pa jiko ilo akuninka Ambuye Mlungu wako.

VI. Usapa.

VII. Usachita chigololo.

VIII. Usaba.

IX. Usamnamizila mnjako pa mlandu.

X. Usakumbila nyumba ya mnanchi wako, usakumbila wamkazi wa mnanchi wako, pena wopotela wake, pena mbumba yake, pena ng'ombe yake, pena mbunda yake, pena chintu chili chonche ali nacho.

Funcho.

Ujiyeluza chiani maka maka pa Matauko aya?

Yanko. Ndijiyeluza vintu viwili: nchito yanga yoyeneledwa kwa Mlungu, ni nchito yanga yoyeneledwa kwa Mnanchi wanga.

Funcho. Chiani nchito yako yoyeneledwa kwa Mlungu?

Yanko. Nchito yanga yoyeneledwa kwa Mlungu, ndiko kumvomela, kumuopa, ni kumkonda ni mtima wanga wa mpumpu, ni njelu zanga zonche, ni umoyo wanga wonche, ni nkongono zanga zonche; kumlambila, kumyamika, ndi kumkulupilila Iye chikulupilile, kumtanila Iye, kuliyinikiza Jina lake la pa loka ni Mau lake, ni kumpotela zene siku zonche za kulama kwanga.

Funcho. Chiani nchito yako yoyeneledwa kwa Mnanchi wako?

Yanko. Nchito yanga yoyeneledwa kwa Mnanchi wanga ndiko kumkonda iye ngati umo ndijikondela namwene, ndi kuwachitila wantu wonche umo ndifunila wakanichitile ine: kukonda, kuyinikiza ni kwatangatila atate wanga ni amai wanga: Kumyinikiza ni kumvela Mfumu, ni wonche awo waninkidwa bwalo panchi pa iye: kujiika pa malo panga panchi pa wonche wakuniongola, woyeluza, wakuniwesa mzimu, ni wene nchito: Kujikonja ni kujichicha ndi kujitimalika pachogolo pa wonche yawo wakupunda msinku wanga: Nisamchitila muntu voipa ingakale pa mau ingakale pa nchito: Kuchita voona ni va malinga pa nchito zanga zonche; Nisakala ni usokolo, kungakale kuipila pa mtima wanga: Kuchekeleza manja yanga,

yangatole tole ni yangabe, lilime langa linganene voipa, ungakale unami, kungakale kuchogoda; Kulisunga tupi langa pa kujisunga, lingapunde, lingakumbile chaje: Nisalilila, misakumbila chuma cha wene; nampo kujiyeluza ndi kupota nchito kwa zene kujipatila namwene kamba, ni kuchita nchito yanga yoyeneledwa pa makalidwe ayo, yapo Mlungu sakakonde kunitanilapo.

Catechist.

Mwana wanga wabwino, ujiwe ichi, kuti sukoza kuchita vintu ivi umwene, sukoza kuyenda enda pa matauko yake Mlungu, ni kumpotela Iye, opanda neema yake yene; iyo sungasie kujiyeluza kuitanicha siku zonche pa kupempela ni likwale. Chimwechi nivele, ngati ukoza kunena Sala la Ambuye.

Yanko.

Atate watu, wa Kumwamba, Jina lako liyelechedwe. Ufumu wako uje. Vija ufuna vichitidwe, mjiko ngati Kumwamba. Utipache lelo chakudya chatu cha siku. Ndi utilekele mangawa yatu, ngati ife tiwalekela wa mangawa watu. Ndi usatitengela poyesedwa; Nampo utipulumuche pa voipa. Amen.

Funcho. Ufuna chiani kwa Mlungu pa Pempeloili?

Yanko. Ndifuna Ambuye Mlungu wanga, Atate watu wa Kumwamba, Wopeleka vonche vabwino, kupeleka neema yake kwa ine, ni kwa makamu yonche; kuti timlambile, timpotele, ni kumvela Iye, umo tiyeneledwela kuchita. Ndi ndimpempa Mlungu, kuti atipelekele vonche ivo vifunidwa pa maumoyo ni matupi yatu; kuti atilengele lisungu, kutilekela zambi zatu: ni kuti alole kutipulumucha ndi kutiombelela ife voluswa vonche pa mzimu ni pa tupi; ni kuti atichekelezele zambi zonche ni mpulipuli, ni wamawongo watu wa pa mzimu, ni kufa kwa vyaka. Ni ichi ndikulupilila kuti sachichite kwa lisungu lake, ni

ubwino wake, mkati mwa Ambuyatu Yesu Kristo. Chifuko chake ndinena, Amen, Chivomelele.

Funcho.

Sakraments zingati Kristo mwene adaikilatu mChurch mwake ?

Yanko. Ziwili zoka, izo zafunidwa ponche ponche kwa kupulumucha wantu ; ndizo Ubatizo, ni Chakudya chogonela cha Ambuye.

Funcho. Mate yanji uli nayo pa mau ili *Sakrament* ?

Yanko. Ndifuna kunena chizindikilo cha kubwalo chakuoneka cha neema ya mkati ya mwa mzimu ipachidwa, choikidwa pa malo pake ndi Kristo mwene, chopanganila cha kulandila imweyo, ndi chogwilizila kutijiwicha kuti tilandila mmwemo.

Funcho. Mbua zingati zilipo pa Sakrament ?

Yanko. Ziwili : chizindikilo cha kubwalo chakuoneka, ni neema ya mkati ya mwa mzimu.

Funcho. Chiyani chizindikilo cha kubwalo chakuoneka, kapena chifa pa Ubatizo ?

Yanko. Maji ; mmwemo mwene wake abatziwa *Pa jina la Atate, ni la Mwana, ni la Mzimu Woyela.*

Funcho. Chiyani neema ya mkati ndi ya mwa mzimu ?

Yanko. Kufela zambi, ni kubadwa kwa chapano pa kuchita malinga : pakuti kuchokela chitulo chatu tinabadwa mzambi, ni wana wa kukwia, mmwemo tachitidwa wana wa neema.

Funcho. Chiyani chifunidwa kwa achinawene wofuna kubatizwa ?

Yanko. Kulapa, mmwemo wasiya zambi chisiile ; ni Mvano, umo wavomelela vija adawalangila Mlungu pa Sakrament ija.

Funcho. Ndipo kwa chiyani makanda wabatizwa, yapo pa kukala wang'ono viwi, sakoza kuyachitilatu ?

Yanko. Pakuti walanga kuchita yonche yawili pakamwa pa Malilinda yao ; chilanga icho sangasie kuchichita achinawene, yapo sadakule.

Funcho. Chifuko chiani Sakrament ya Chakudya chogonela cha Ambuye idaikidwa pa malo pake ?

Yanko. Kuchita chikumbu kumbu wosapuma cha nchembe ya kufa kwake Kristo, ni vija vokomela tilandila mmwemo.

Funcho. Chiani mbua ya kubwalo kapena chizindikilo cha Chakudya chogonela cha Ambuye ?

Yanko. Mkate ni vino, ivo Ambuye adataukila tivilandile.

Funcho. Chiani mbua iyo ya mkati, pena icho cholangizidwa ?

Yanko. Tupi ni Mwazi wake Kristo, ivi wakuvomela wavitenga ni wavilandila zene pa Chakudya chogonela cha Ambuye.

Funcho. Chiani vakutikomela pa ivo titapa pa imweyo ?

Yanko. Kuyalimbicha ni kuyabwezela mpavu maumoyo yatu kwa Tupi ni Mwazi wa Kristo, umo matupi yalimbichidwila kwa Mkate ni Vino.

Funcho. Chiani chifunidwa kwa awo wachijela Chakudya chogonela cha Ambuye ?

Yanko. Kujilinga wene, ngati walapa zene kwa zambi zao za kale, ni kupanga njelu wosakaikila kuchata umoyo wa chapano ; kukala ni Mvano wa chilamile mmalisungu yake Mlungu mkati mwa Kristo, pamoji ni kukumbukila chiyamikile umo adafela ; sonincho kukala pa chikondano ni wantu wonche.

¶ *Wosungila wa Paroikia lili lonche, pa Siku za Ambuye ni pa Sika zoyera, pambuyo pa Somo la kawili, ajiwayeluza ni kwalinga pa danga pa Church, wana wa Paroikia lake yawo sapelekedwe kwa iye, umo iye saone kuti ikomela, pa mbua ina ina ya Catechism ii.*

¶ *Ni Achatate wonche ni Achamai ni Wene nchito, ingakale wamuna, ingakale wakazi, wayendeche Wana*

wao, Wopotela ni Apprentices (yawa sanajiyeluza Catechism yao,) ku Church, pa nyengo yolangizidwa, ndi wavere popanda mtafu, ndi waikidwe pa malo pao ni Wosungila, mpaka sakate kujiyeluza vonche ivo volangizidwa apa kuti wajiyeluze.

¶ *Chapano apa Wana awa sakafikile msinku wakukozela, ndi wakoza kunena, pa mau ya Achamaye, Mvano, Sala la Ambuye, ni Matauko kumi, ni sonincho sakoze kuyankila mafuncho yena ya Catechism yofupika ii, wajitengedwa kwa Askof. Ndi ali yenche ajikala ni Atate kapena Amai ngati wa pa Ubatizo kukala Mmboni wa kulimbichidwa kwao.*

¶ *Ndipo pali ponche Askof sajiwiche kuti Wana watengedwe kwake kwa kulimbichidwa kwao, Wosungila wa Paroikia lili lonche kapena ajitenga, kapena apeleke yalembedwa, ni janja lake mwene lilembe panchi, majina ya achinawene wonche mParoikia lake, yawo saganize kuti atuluchidwe kwa Askofu walimbichidwe. Ndi, ngati Askof akawaloleza, ajiwalimbicha umo yachatilamo.*

KAKONJEDWE KAKE

CONFIRMATION,

KAPENA KWATILA MANJA YAWA WOBATIZWA NDI WAFIKILA MSINKU WA WENE NJERU.

¶ *Pa siku ilo lalangizidwa, wakakala pa malo pake wonche yawo wafuna kutilidwa manja, chiimile pa mpambo pachogolo pa Askof: ndi iye (kapena Wotumikila Mlungu mwina uyo agwirizidwa naye) ajiwerenga mau aya yakuyambila yachatayo.*

Dala kuti Confirmation lichitidwe kumtumikila Mlungu kwa kupunda kumangicha bwino yawo siwalilandile, Church laona bwino kutauka kuti, Namba muntu sakoze kulimbichidwa chiyambile lelo, ikawe yawo wakukoza kunena Mvano, Sala la Ambuye, ndi Matauko kumi; sonincho kuyanka mafuncho yena, umo yalembedwela mKatekisimo lofupika: tauko ili kulinganicha viwi kuligwila: dala wana wakafikila msinku wa wene njelu, ndi wakata kujiyeluza ivo wadalanga achatate ndi amaye kwa achi iwo pa Ubatizo, achinawene, pa kamwa pao ndi kwa kutanikila kwao, pa danga pa Church, wavomeleze ndi kulimbicha mau yamweyo; sonincho dala walange kuti, kwa neema yake Mlungu, siku zonche sayese kuyasunga kwa kuvomeleka mau aya, umo pa kuvumbula kwao achinawene wadatanikila.

¶ *Ndipo sajinena Askof,*

Kodi mlangancho nditu, ndi kulumbilila, pa maso pa Mlungu, ndi Gulu ili la Church, aya yadachitika

pa jina lanu pa Ubatizo wanu : kuvomelezancho ndi kulimbicha mau yamweyo inu mawene, ndi kujijiwicha kuti mwamangidwamo kuvomela ndi kuyachita, aya yonche achatate ndi achamanu wa pa Ubatizo wadalanga uko pa mlandu wa inu ?

¶ *Ndipo ali yenche ajiyanka ndi mau loveka,*

Ndilangancho.

Askof.

Matangatidwe yatu yali pa Jina la Ambuye.
Yanko. Uyo wapanga kumwamba ndi jiko.
Askof. Liyelekedwe jina la Ambuye ;
Yanko. Chiyambile lelo mpaka vyaka vosatela.
Askof. Ambuye, mvele mapempelo yatu.
Yanko. Ndi chililo chatu chikufikileni.

Askof. Tipempe.

Mlungu mwene mpavu zonche wa chilamileje, Mwalola kwabalancho yawa wopotela wanu kwa Maji ndi Mzimu woyela, ndi Mdawapacha kulekela zambi zao zonche ; mwalimbiche tikupembezani, Ambuye, ndi Mzimu woyela Woimilila, ndi siku ndi siku mwaonjezele va chomwe vanu va neema va mitundu mitundu ; mzimu wa njeru ndi wa kuzindikila ; mzimu wa umbili ndi chimuna cha pa mzimu : mzimu wa kujiwa ndi kulambila kwa zene ; ndi mwazaze, Ambuye, ndi mzimu wa manta yanu yakuyelecha, chapano ndi vyaka vonche. *Amen.*

¶ *Ndi wonche wakagwada pa mpambo pachogolo pa Askof, iye ajitila janja lake pa mutu wa ali yenche mmoji mmoji, nikuti,*

Sungani Ambuye, uyu Mwana wanu [pena *uyu Wakupotela wanu*] ndi neema yanu ya kumwamba, akaliletu wanu kwa vyaka ndi vyaka ; ndi aonjezeke

kupunda siku ni siku pa Mzimu wanu woyela, mpaka afikile ufumu wanu wa vyaka. Amen.

¶ *Ndipo Askof ajinena,*

Ambuye akale ndi inu.

Yanko. Akale ndi mzimu wanu.

¶ *Ndi (wonche chigwadile) Askof ajiongezela,*

Tipempe.

Atate watu, wa Kumwamba, Jina lako liyelechedwe. Ufumu wako uje. Vija ufuna vichitidwe, mjiko ngati Kumwamba. Utipache lelo chakudya chatu cha siku. Ndi utilekele mangawa yatu, ngati ife tiwalekela wa mangawa watu. Ndi usatitengela poyesedwa ; Nampo utipulumuche pa voipa. Amen.

¶ *Ndi Pempelo ili la chidule.*

Mlungu Mwene mpavu zonche wa umoyo wosatela, wakutipacha kukumba ndi kuyachita aya yali yabwino ndi yaloleka pa maso pa Ukulu wanu ; Ife tikupembezani kwa kujichicha pa mlandu wa yawa wopotela wanu, pamwamba pao tatila manja, (kuchata mlingo wa aApostolo wanu woyela) kuwajiwicha iwo (kwa chizindikilo ichi) kuti mwalola ni ubwino wanu wene neema. Janja lanu la chitate, tikupembezani, likale chikalile pamwamba pao ; Mzimu wanu Woyela akale nawo chikalile ; ndi mwachogoze pa kulijiwa ndi pa kulivela Mau lanu, mpaka potela pake wakupatile kulama kwa vyaka ; kwa Ambuyatu Yesu Kristo, uyu pamoji namwe ndi Mzimu Woyela akala ndi kulamula, Mlungu mmoji, vyaka vosatela. *Amen.*

Ambuye mwene mpavu zonche, Mlungu wa vyaka vonche, mlole, tikupembezani, kuchogoza, kuyelecha, ndi kuongola, mitima ndi matupi yatu pa njira ya mau yanu, ndi nchito za matauko yanu ; ndipo mkatisunge ndi mpavu zanu zoyenela nditu pano ndi kwa

vyaka, tilindilidwe pa tupi ndi pa umoyo ; kwa Ambuyatu ndi Mpulumuchi watu Yesu Kristo. *Amen.*

¶ *Ndipo Askof sajiwapacha mwawi, kunena chimwechi,*

Mwawi wa Mlungu Mwene mpavu zonche, Atate, ndi Mwana, ndi Mzimu Woyela, ukale pa inu, ndi kulongeza ndi inu kwa vyaka vonche. *Amen.*

¶ *Namba muntu salovyedwe pa Kusanganizana Kuyela, mpaka akatilidwe manja, kapena akakale woikidwilatu ndi wofunilatu kutilidwa manja.*

CHIFA CHENE CHA

KUCHITICHA UKWATI PA WOKA.

¶ *Pachogolo, sangasie kubukicha pa bwalo pa Church masiku ya Ambuye yatatu pa loka pa loka Banns ya wonche wakuungidwa pamoji pa Ukwati, pa nyengo ya Sala za Umawa, kapena pa Sala za Ujulo, (ngati palije Sala za Umawa,) mkutaje Somo la kawili ; Wakusunga kunena, umo wamanenela vyaka,*

Ndibukicha Banns za ukwati pakati pa *M.* wa pa— ndi *N.* wa pa —. Akakala pano muntu wa inu wakujiwa chifuko kani chintu cha malinga cha kuwalekecha wantu awa wawili angalunjane pa Ukwati woyela, mkadaonecha. Iyi ni nyengo ya kuyamba [*yakawili*, pena *ya katatu*] ya kufuncha.

¶ *Ikakala kuti achinawene awa wakukwatana wakalapo pa Paroikia pena pena, sajibukicha Mau ya kunena pa bwalo Ukwati kufunchila pa miji yonche iwili. Ndi Wakusunga yuja pa Paroikia limoji sakadachiticha Ukwati pa woka, akapanda kulandila kalata yakujiwicha ya Wakusunga pa Paroikia linjake yakuti adabukicha katatu Banns.*

¶ *Pa siku ndi nyengo zija zidalangizidwapo za kuchiticha Ukwati pa woka awa wakukwatichidwa sajiloa pakati pa Church pamoji ndi achabwenji wao, ndi wantu wa pa miji yao : ndi kuima pamwepo, wamuna pa janja la chimuna, ndi wamkazi janja la manjele, Kasis sajinena.*

Wokondedwa viwi, tasonkana pano pa nkope ya Mlungu, ndi pa nkope ya gulu la Church pano, dala kuunganicha Wamamuna uyu ndi Wamkazi uyu pa Ukwati wa pa woka; ndiyo makalidwe yolemekezedwa, yaja adaikilatu Mlungu, pa nyengo ya wana wa adam wakali wosalakwa, kutizindikilicha umo Kristo ndi Church lake wachitidwila pamoji kuseli; makalidwe aya ya pa yoka Kristo adapamba ndi kuyakadwicha pa kukalapo mwene, ndi pa chizindikilo icho chakuyamba adachita, pa Kana ya Galili; ndi Woyera Paolo adayalolecha kuti ndi makalidwe yakulemekezedwa pakati pa wonche: ndi chifuko ichi muntu ali yenche sakadajigwiriza Ukwati uu, ingakale sakadayamba, wakali wosapangana njelu, ngati chintu chaching'ono, ndi chakukupizana, kukuticha makumbilo ya nyama ya wana wa adam ndi ivo wangojifunila, ngati vikoko vosali ndi malango; nampo wakadachita ndi ulemu ndi malango, kupanga bwino njelu, ndi kwa kujisunga, ndi kumuopa Mlungu; chiganizile umo muyeneledwela vifuko vija adaviikilatu Mlungu Ukwati.

Poyamba, udaikidwa pa malo pake kwa kubala wana, waleledwe pa kumuopa Ambuye ndi pa malelo yake, ndi walilumbe Jina lake loyera.

Pa chiwili, udaikidwa pa malo pake chifa cha mankwala ya zambi, kulewa vyasa; kuti achinawene yawo wosali ndi neema ija ya kujisunga wakwatane, wajisunge viwalo vopanda ukazuzi va tupi lake Kristo.

Pa chitatu, udaikidwa pa malo pake kwa kuyanjana ndi kutangatilana, ndi kutontozana, umo mmoji akadakalila ndi mnjake, pa nyengo za kufanikila ndi za kufinikizidwa. Pa makalidwe aya wakuja waungidwe chapano achinawene yawa wawili wali pano. Chimwechi akakala muntu akoza kulangiza ndande ya malinga ili yonche chifuko chake yawa sakadaungidwa pamoji, anene chapano, pena asanena vyaka vonche.

¶ *Sonincho, kukamba ndi achinawene awo sakwatichidwe, ajinena,*

Ndikufunchani ndi kukuombelezani inu mawonche wawili umo simyankile siku lija lene manta la milandu, yapo vobisalika va pa mitima yonche sivivunukulidwe, ngati mmoji wa inu akajiwa chintu chakulekecha, mngaunganichidwe bwino pa Ukwati, umo mutaukidwila ndi bwalo, chivumbuleni chintu ichi chapano. Chifuko jiwichani bwino, kuti wali wonche yawo wakaunganichidwa mwina umo mosaloleka pa Mau la Mlungu, yawa wasaunganichidwa ndi Mlungu; ndi ukwati wao wosali wotaukidwa ndi bwalo.

¶ *Pa siku iyo ya Ukwati, muntu akatulucha ndi kukumbiliza chili chonche ndande ya kuchekeleza, kuti sakadaungichidwa pa Ukwati kwa mlingo wa Torah ya Mlungu, ingakale kwa mlingo wa Torah za Ufumu; ndipo akalola kwapelekela yawo wa ukwati chogwirizila, choyenela, pamoji ni wena malilinda wakuyanka; (kapena saike chuma chosachepekedwa kulipililatu chuma chao chingawataike yawa wa Ukwati,) kuti salimbiche aya ayakumbilizayo: ndipo kuchita Ukwati kwa pa woka ujipwechedwa, mpaka ya zene ya mau aya siyanenedwe.*

¶ *Akapanda muntu kukumbiliza chakuchelelezа, ndipo Wakusunga sajiti kwa Wammuna,*

M. Ufuna kukala ndi wamkazi uyu pa Ukwati akale mkazako kwa mlingo ya torah, pa makalidwe aya ya pa yoka ya Ukwati? Ufuna kumkonda, kumtontoza, kumlemekeza, ndi kumsunga bwino pa kudwala nti pa kusangalala; sonincho, kwaleka wena wonche, kukala naye iye yeka, inu mawonche mkakala ndi umoyo?

¶ *Wammuna ajiyanka,*

Ndifuna.

¶ *Ndipo Kasis ajiti kwa Wamkazi,*

N. Ufuna kukala ndi Wamwamuna uyu, akale mwamunako kwa mlingo wa torah, pa makalidwe aya ya pa yoka ya Ukwati? Ufuna kumvecha, kumpotela, kumkonda, kumlemekeza, ndi kumsunga bwino pa kudwala ndi pa kusangalala; sonincho, kwaleka wena wonche, ndi kukala naye iye yeka, inu mawonche mkakala ndi umoyo?

¶ *Wamkazi ajiyanka,*

Ndifuna.

¶ *Ndipo Wotumikila Mlungu ajinena,*

Yani apeleka wamkazi uyu, akwatiwe ndi Wamamuna uyu?

¶ *Ndipo wawili awa wajitomeleza mvano chimwechi.*

Wotumikila Mlungu, nalandila Wamkazi pa manja ya atate wake kapena nkoswe yake, ajimgwilicha Wammuna janja lake la chimuna Wamkazi janja lake la chimuna, ndi ajimnenecha kuchaticha kunena kuti.

Ine *M.* ndikutengani imwe *N.* kukala mkazanga kwa mlingo wa torah, ndikale namwe ndi kugwila chiyambile lelo, mkafanikila mkafinikizidwa, ndimngapunde kulemela ndimngapunde kukala mpawi, ingakale mkadwala ingakale mkasangalala, kukonda ndi kusunga, mpaka kufa kukatipatula, kwa mlingo wa maikidwe yake yoyela Mlungu; ndimo mmwemo ndikutomelani mvano wanga.

¶ *Ndipo wajitaizana manja yao; ndi Wamkazi, ndi janja lake la chimuna kumgwira Wammuna janja lake la chimuna, sajiti chimwechija kumchaticha Wotumikila Mlungu,*

Ine *N.* ndikutengani imwe *M.* kukala mwamunanga kwa mlingo wa torah, ndikale namwe ndi kugwira, chiyambile lelo, mkafanikila mkafinikizidwa, ndimngapunde kulemela, ndimngapunde kukala mpawi, ingakale mkadwala ingakale mkasangalala, kukonda, kusunga, ndi kuvecha, mpaka kufa kukatipatula, kwa mlingo wa maikidwe yake yoyela Mlungu; ndimo mmwemo ndikutomelani mvano wanga.

¶ *Ndipo sajitaizanancho manja yao: ndi Wamwamuna ajimvalika Wamkazi Linawila, kuliika limwelo pamwamba pa chikalakala pamoji ndi chintu kwa chisimucha kumlipilila Kasis ndi mKleriko wake. Ndipo Kasis, kulitenga Linawila, sajilipeleka kwa Wamwamuna, alitile pa chala cha kanai cha janja la manjele la Wamkazi. Ndipo Wamwamuna akaligwila Linawila pamwepo, ndi Kasis chimyeluzile, sajiti,*

Ndi Linawila ili ndikutomelani, ndi tupi langa ndikuyinikizani, ndikuvekani ndi vonche ivo ndili navo pa jiko lino: Pa Jina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyela. Amen.

¶ *Ndipo Wammuna nakasia Linawila pa chala cha kanai cha janja la manjele la Wamkazi, wonche wawili wajigwada; ndi Wotumikila Mlungu sajiti,*

Tipempe.

Mlungu wa chikalileje, Wakupanga ndi Wakusunga wana wa adam wonche, Wakupacha neema yonche ya mwa mzimu, Wakuyambiza kulama kwa vyaka; Mpeleke mwawi wanu pa awa wopotela wanu mwamuna uyu ndi wamkazi uyu, yawo tiwapacha mwawi pa Jina lanu; kuti umo Isaak ndi Rebeka wadakalila ndi umoyo pamoji chivomelekele, chimwechi achinawene yawa wachitiletu ndi kusungilatu aya wadayalumbila ndi malangano yochitidwa

pakati pao, (Linawila ilo wadalipacha ndi wadalilandila ndilo chizindikilo ndi chogwilizira chake) ndi walongeze vyaka vonche pakukondana chikondanile ndi mtendele nditu, ndi wakale ndi umoyo wao kwa mlingo wa torah zanu; mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

¶ *Ndipo Kasis aiigwilanicha manja yao ya chimuna, ndi sajiti,*

Yawo Mlungu waungichana pamoji, muntu asapatula.

¶ *Ndipo Wotumikila Mulungu ajiwanenela kanu.*

Pakuti *M.* ndi *N.* wavomelezana pamoji waloe pa ukwati woyela, ndi walangiza umboni chimwechi pa maso pa Mlungu ndi yawo wosonkana pano, ndi mmwemo wadatomeleza mvano wao uyu ndi mnjake, ndi walangiza chimwechi kwa kupeleka ndi kulandila Linawila, ndi pakugwilana manja; Ndikubukicha pa bwalo kuti yawo wali wamuna ndi wamkazi pamoji, pa Jina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyela. Amen.

¶ *Ndipo Wotumikila Mlungu sajiongezela mau aya yakupacha Mwawi.*

Mlungu Atate, Mlungu Mwana, Mlungu Mzimu Woyela, akuninkeni mwawi, akulindilileni, akusungeni; Ambuye ndi lisungu lake akupenyeni chilolele; akuzazeni ndi mwawi wonche wa mwa mzimu ndi neema, mpaka mkale pamoji pa umoyo uu wa panchi pano, dala mkale ndi kulama wa chikalile mmwemoje kwa vyaka ivo sivije. *Amen.*

¶ *Ndipo Wotumikila Mlungu kapena wa Kleriko, nakamukila ku Meza ya Ambuye, sajinena kapena sajiimba Zabur iyi ichatayo,*

Beati omnes. Zabur cxxviii.

Wakusengwa ali yenche wakumwopa Ambuye: ndi wakuyenda pa njila zake.

Suvidye vakulema va vyala vako: wakusengwa iwe, ndi chabwino kwako.

Mkazako ngati mpelesa wopacha: kukati kwene kwa nyumba yako;

Wana wako mbeu za mtengo wa mizeit: chizungulile meza yako.

Penya, pakuti chimwechi sapachidwe mwawi: wamamuna uyo wakumwopa Ambuye.

Ambuye sakupache mwawi kuchoka pa Zion: ndi sukaone Yerusalem pabwino masiku yonche ya chilamile chako;

Yetu, suone wana wa wana wako: ndi mtendele pamwepo pa Israel

Akuzike Atate, ndi Mwana: ndi Mzimu Woyela;

Umo kumakilila poyamba, chimwechi ndi chapano: ndi kwa vyaka vosata. Amen.

¶ *Pena Zabur vi.*

Deus misereatur. Zabur lxvii.

Mlungu atichitile neema, akatipache mwawi: amulikiche nkope yake kwa ife;

Njila yako ijiwike muno mjiko; upulumuchi wako pa mafuko yonche.

Makamu yabukiche mbili yako, Mlungu: yabukiche mbili yako makamu yonche.

Vilawa viseke vikalulute: chifuko suyalamule makamu chiongokele, ni suvichogoze vilawa pa jiko.

Makamu yabukiche mbili yako, Mlungu: makamu yonche yabukiche mbili yako.

Jiko lavipeleka vipacho vake: Mlungu, Mlungu watu, satipache mwawi.

Mlungu satipache mwawi: ndi vinchonga vonche va jiko sivimwope.

Akuzike Atate, ndi Mwana: ndi Mzimu Woyela;

Umo kumakalila poyamba, chimwechi ndi chapano: ndi kwa vyaka vosata. Amen.

¶ *Ndi ikata Zabur, Wammuna ndi Wamkazi chigwadile pachogolo pa Meza ya Ambuye, Kasis chiimile pa Meza, nang'anamula nkope yake kwao, ajinena,*

Ambuye, atilengele lisungu.
Yanko. Kristo, atilengele lisungu.
Wotumikila. Ambuye, atilengele lisungu.

Atate watu, wa Kumwamba, Jina lako liyelechedwe. Ufumu wako uje. Vija ufuna vichitidwe, mjiko ngati Kumwamba. Utipache lelo chakudya chatu cha siku. Ndi utilekele mangawa yatu, ngati ife tiwalekela wa mangawa watu. Ndi usatitengela poyesedwa; Nampo utipulumuche pa voipa. Amen.

Wotumikila. Ambuye, mpulumuche kapolo wanu, ndi mbumba yanu.
Yanko. Yawo wakukupililani.
Wotumikila. Ambuye, mwapelekele kutangatila kuchoka pa malo panu poyera;
Yanko. Ndi vyaka vonche mwalindilile.
Wotumikila. Mkale kwa awa ngati linga la mpavu.
Yanko. Pa maso ya awo wakuwaipila.
Wotumikila. Ambuye, mvere mapempero yatu.
Yanko. Ndi chililo chatu chikujeleni.

Wotumikila Mlungu.

Mlungu wa Abraham, Mlungu wa Isaak, Mlungu wa Yakobo, Mwapache awa akapolo wanu mwawi; Mkavyale mbeu ya kulama kwa chikalileje mmitima yao; kuti vili vonche ivo vakuwakomela sajiyeluze pa Mau lanu loyela, wavimalize vimwevo pa kuchita. Mwapenyele ni lisungu, Ambuye, kuchokela kumwamba, mkawapache mwawi. Ndi umo mdawapelekela Abraham ndi Sarah mwawi wanu, kuwatontoza viwi, chimwechi mlole kuwapelekela mwawi wanu

awa akapolo wanu; kuti yawa pa kuvecha ivo mfuna, ndi chikalile posaluswa mkawavinikila, walongeze mkukonda kwanu mpaka potela pake maumoyo yao; mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

¶ *Pempelo ili lakuchata lijisiidwa, yapo Wamkazi wata kupita nyengo ya kubala mwana.*

Ambuye wa lisungu, ni Atate wa Kumwamba, kwa mninko wanu wene neema wana wa Adam waonjezeka; Tikupembezani, mwatangatile ni mwawi wanu awa wawili achinawene, wapachane pakupuma wana, sonincho wakale ndi umoyo wao pamoji mkukondana bwino pa maso yanu, ndi mbili yabwino, mpaka sakaone wana wao wakwabala, kuti waleledwe kwa mlingo wa wa-Kristo ndi wa ubwino wa chimamuna, dala wakulumbeni ndi wakulemekezeni; mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

Mlungu mdapanga vintu vonche kwa kuyenela kwa mpavu za chimuna zanu, yapo padalije kantu; ndi sonincho (mkate kuyakonja mau yena) mdalangizilatu kuti kutapa pa wamuna (wopangidwa pa chitunjitunji chanu ndi kufwanana nanu) wamkazi ajipatile kuyamba kwake; ndi pa kwamangizanicha mmwayaluza sikungaloleke ndi bwalo chikalileje kwapatula yawa mdawachita wakale amoji pa ukwati: Ee Mlungu, mwayaika pa yoka makalidwe ya ukwati kukala mau la kuseli lopambana, chizindikilo chakulangiza ukwati wa pa mzimu ndi umoji uwo ulipo pakati pa Kristo ndi Church lake; Mwapenyele ndi lisungu yawa akapolo wanu, kuti wamwamuna uyu amkonde mkazake kwa mlingo wa Mau lanu, (umo Kristo adamkondela mkazake Church, naye adijipeleka pa milandu yake, nakalikonda nakazowekana nalo bwino, ngati ni nyama ya Iye yeka), sonincho kuti wamkazi uyu akale wakukonda ndi wakukondeka, wakuvomeleka ndi wakumvecha ma-

munake, ndipo achate mlingo wa achamaye woyela wakumuopa Mlungu, pakuzika mtima pa kujisunga bwino ndi pa mtendele. Ambuye, mwapache mwawi yawo wonche wawili; mkawapache waloe pa ufumu wanu wa vyaka chokolo, kwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

¶ *Ndipo Kasis ajinena,*

Mlungu mwene mpavu zonche, uyo pa kuyamba adapanga waja wakutibala wa pachogolo, Adam ndi Hawa, ndi adawaika pamoji mukwati; akupungulileni chuma cha neema yake, akuyelecheni, akupacheni mwawi, mumkondweche pa tupi ndi pa umoyo, mkakale pamoji mkukondana kuyela mpaka potela pake maumoyo yanu. *Amen.*

¶ *Pambuyo pake, ngati palije Sermon yakubukichila nchito zoyeneledwa za Wammuna ndi Mkazake Wotumikila Mlungu sajiwerenga mau aya yachatayo.*

Inu monche mwakwata, pena wali ni mtima kujilovya pa makalidwe ya pa yoka ya Ukwati, verani aya yanena Malembo yoyela kuti wamuna wakadawachitila akazao, ndi wakazi wakadawachitila amunao.

Paolo Woyela, mEpistola mwake kwa wa Efeso, pa chapter ya kasano, awapacha tauko ili wamuna wonche wokwata; Wamuna akondeni achakazanu, umo Kristo adakondela Church, adajivumbula pa milandu yake, aliyereche ndi kulichuka, kwa kulisavya mmaji, kwa Mau lake; ajituluchile Church lokuzika, losali ni banga, ingakale chinya, ingakale chintu chinancho chimwechi; nampo likakale loyela, losali lakudecha. Chimwechi wamuna wali ni mangawa ya kulipa kwakonda akazao ngati matupi yao wene. Uyo amkondayo mkazake ajikonda mwene: chifuko palije muntu nyengo ili yonche adaipila nyama yake mwene, nampo ailela bwino ndi kuzewelela nayo ngati lifowe, umo Ambuye ndi Church: pakuti tili viwalo va tupi lake, va nyama yake, ndi vifupa vake. Kwa chifuko ichi

muntu sajileka Atate wake ndi Amake, ndi sajikumbatilana ndi mkazake; ndi yawo wawili sapate kukala nyama imoji. Aya ni mau ya kuseli yakulu; ine nampo ndimnena Kristo ndi Church. Nampo inu pali ponche mmoji mmoji amkonde mkazake, ngati umo ajikondela mwene wake.

Chimwechija mmweyuja Paolo Woyela, pakuwalembela wa Kolosse, akuti chimwechi kwa wonche wokwata; Wamuna, mwakonde akazanu, musawawa nawo pa mtima.

Velanincho ayo Petro Woyela, Apostolo wa Kristo, naye wokwata mwene, awanenela waja wakwata: Inu wamuna, kalani pa nyumba kwa mlingo wa kuzindikila pamoji ndi akazanu; kumgawila ulemu wamkazi, ngati katundu wochepa mpavu, ngati wakuloa chokolo cha neema ya kulama pamoji nanu, kuti sala zanu zisachekelezedwa.

Mpaka pano mwavela nchito yoyeneledwa ya wammuna kwa mkazake. Sonincho inu wakazi, velani ndi jiyeluzeni nchito zanu zoyeneledwa kwa amunanu, ngati umo zalangizidwilatu pa danga pa Malembo yoyela.

Paolo Woyela, pa Epistola ija yochulidwa pachogolo kwa wa Efeso akuyaluzani chimwecho; Wakazi, mjiike pa malo panchi pa wamuna wa inu moka, ngati panchi pa Ambuye. Chifuko wamuna ndi mutu wa wamkazi, ngati Kristo ndi mutu wa Church: ndi iye Mpulumuchi wa tupi. Mmwemo ngati umo Church lijiikila panchi pa Kristo, achiwakazi wakale chimwechija panchi pa achamuna wao. Anenancho, Wamkazi ajikalila ni manta pa mamunake.

Ndi mEpistola mwake kwa wa Kolosse, Woyela Paolo akupachani yeruzo lalifupi; Achiwakazi mjiike pa malo panu panchi pa wamuna wanu, umo mufwanikila pa Ambuye.

Petro ncho Woyela, akuyaluzani ya bwino nditu kuti chimwechi: Inu wachikazi, mjiika pa malo panu panchi pa wamuna wa inu moka; dala ngati wena

wakakala wopanda kunyengeka ndi Mau, kwa makalidwe ya wakazi watengedwe ngati chipatapata wopanda Mau; nakakala amboni wa makalidwe yanu yoyerechedwa yene manta. Kupamba kwanu kosali ni kupika chichi, pena kuvala gold, pena kujiveka malaya yena yena; nampo kujipamba muntu kwa kuseli pa mtima, ndi vintu vosali vakuonangika; ndio kupamba ndi mzimu wodeka ndi wa mtendele; ndio wa mtengo wonyinji pa maso pake Mlungu. Chimwechi kale achiwakazi woyela wakumkulupilila Mlungu adajikonja, kujiika pa malo ya panchi pa wamuna wa achiiwo woka; umo Sara adamvechela Abraham, kumtana Ambuye; wa uyo mdapata kukala wana mkakala chichitile va bwino, ndi wosaopa kuzizwicha.

¶ *Chalinganicha kuti yawo wakwatana wajilandila Kusanganizana Koyela pa nyengo ya Ukwati wao, pena yapo sakaone nyengo ya kuyamba pambuyo pa Ukwati wao.*

KAIKIDWE KA

KUMJELA CHIPENYELELE UYU ALIJE MPAVU MTUPI.

¶ *Yapo muntu akadwala, wakadmuulila Wotumikila Mlungu wa Paroikia; naye, pa kuloa pa nyumba ya uyo alije mpavu mtupi, ajiti,*

Mtendele kwa nyumba ii, ndi wonche yawo wakalamo.

¶ *Mkuloaje kuonana ndi uyo alije mpavu mtupi pa kugwada panchi ajiti,*

Msakumbukila, Ambuye, vochwalicha vatu, ingakale vochwalicha va achatate watu wa kale; Mtilekele, Ambuye wabwino, mlilekele kamu lanu, ilo mdaliombola ndi mwazi wanu wene mtengo woukulu, ndi msakwia ndi ife, kwa vyaka va chikalile.

Yanko. Mtilekele ife, Ambuye wabwino.

¶ *Ndipo Wotumikila Mlungu ajiti,*

Tipempe.

Ambuye, mtilengele lisungu.
Kristo, mtilengele lisungu.
Ambuye, mtilengele lisungu.

Atate watu, wa Kumwamba, Jina lako liyelechedwe. Ufumu wako uje. Vija ufuna vichitidwe, mjiko ngati Kumwamba. Utipache lelo chakudya chatu cha siku.

Ndi utilekele mangawa yatu, ngati ife tiwalekela wa mangawa watu. Ndi usatitengela poyesedwa ; Nampo utipulumuche pa voipa. Amen.

Wotumikila. Ambuye, mmpulumuche kapolo wanu ;
Yanko. Uyo akukulupililani.
Wotumikila. Mmpelekele matangatilo kuchoka pa malo yanu pa yoka ;
Yanko. Ndi umwombelele vyaka va chikalileje ndi mpavu.
Wotumikila. Wakuipila asajipatila kantu pa iye ;
Yanko. Angakale woipa asawandikila kumluma.
Wotumikila. Mkale kwake, Ambuye, nyumba ya kuyenda mmwamba ya mpavu.
Yanko. Pa maso ya mawongo ndi iye.
Wotumilika. Ambuye, mvele mapempelo yatu.
Yanko. Ndi chililo ckatu chikujeleni.

Wotumikila Mlungu.

Ambuye, kuchokela Kumwamba zuzumilani panchi, penyani, mmjele chipenyelele ndi kumpumicha nyu kapolo wako. Mmpenye ndi maso ya lisungu lanu, mmtontoze ndi kumkulupililicha chikulupililile kwanu, mmwombelele kuluswa kwa wakuipila, mmsunge iye pa mtendele wosapuma popanda vipandu ; mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

Mtivele ife, Mlungu Mwene mpavu zonche, ndi mwene lisungu lakupunda, ndi Mpulumuchi ; mtambasule ubale wanu umo mmachitila vyaka pamwamba pa uyu kapolo wanu, uyo apwetekechedwa ndi kukala wopanda mpavu mtupi. Chonde mukaike pa koka kulanga kwanu kwa chitate ; ndipo pakuva umo achepekedwela mpavu mtupi apunde kupata mpavu pa kuvomela, ndi kulapa kosamala : Dala kuti, mkakonda kumpacha ncho kusangalala ngati kale, akale ndi umoyo chiyambile chapano pa kukuopani, jina lanu likuzidwe mmwemo : pena mmpache neema

apate kulandila kulanga kwanu, kuti pambuyo pake umoyo uu wakupwetekecha ukata, alongeze pamoji ndi imwe pa kulama chikalile mmwemoje ; mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

¶ *Ndipo Wotumikila Mlungu ajichisa uyo alije mpavu mtupi pa mau aya, pena yena yakufwanana.*

Wokondedwelatu, ujiwe ichi, kuti Mlungu Mpavu yene ali Ambuye wa kulama, ndi Ambuye wa nyifa, ndi wa vonche vija vili vao, ngati ubwana, mpavu, kusangalala, kukota, kulenda, ndi kudwala. Mmwemo ujiwe wosakaikila kuti monche monche umo udwalilamo, Mlungu mwene ali mkukujela chipenyelele. Ndipo ndande yake ikakala yonche yonche kuti kudwala uku kutumidwa kwako ; kukakala kutulucha umo ukozela kujizinga chifa cha mlingo uwo wena wakadauchanja, ndi kuti kuvomela kwako kutuluchidwe pa siku la Ambuye chintu chakulumbika, cha kukuzika, ndi chakulemekezedwa, mmwemo kuonjezela kukuzika, ndi chimwemwe chosatela ; kapena kanatumidwa kwako dala kulanga ndi kukonja pa iwe chili chonche icho maso ya Atate wako wa Kumwamba yachimwa nacho ; ujiwe wosakaikila, kuti ukalapa chilapile kwa zambi zako, ndi kujizinga pa kuva kudwala kwako chikulupilile pa lisungu la Mlungu, chifuko cha Mwana wake wokondedwa Yesu Kristo, ndi ukamyamika kujichicha pa kuja kwake kwa chitate chipenyelele, kujiika pa malo pako panchi pa iye monche monche umo afunila, utenda uu siukung'anamukile kukukomela, ndi kukuchogoza chitangatile pa njila yoongoka yakuchogoza ku kulama chilamileje.

¶ *Muntu wakupenyeledwa akadwalicha, Wosungila akoza kudula mau yake ya kuchisa yapa, pena ayende mchogolo.*

Mmwemo usazizwa ndi kulanga kwake Ambuye Chifuko (umo Woyela Paolo anenela pa Chapter ya

kumi ndi chiwili kwa wa Eber) ali yenche Ambuye amkonda amlanga: ndi amtyapula mwana ali yenche uyo amlandila. Mkajizinga ndi kulanga, Mlungu akuchitilani chifa cha wana; pakuti mwana wanji uyu atate wake wosamlanga? Nampo mkakala popanda kulangidwa, yapo wonche wapata kukala wene mbua, ndipo muli wa mtengo, wosali wana. Ndi mpambo, tidakala ndi achatate watu wa pa nyama yatu, yawo wadatilanga, ndipo tidawayinikiza: nanji sitikadajiika pa malo patu panchi pa Atate wa mizimu ndi kulama? Pakuti yawo zene wadatilanga kuloza pa siku zowelengeka kwa mlingo wa kuwaonekela bwino achinawene; nampo iye dala kutikomela, tipate mbua pa kuyela kwake. Mau yaya, *mbale* wabwino, yalembedwa pa Malembo ya pa yoka dala kutitontoza ndi kutiyeluza; kuti chijizingile, ndi chiyamikile, tivele kulangidwa ndi Atate watu wa Kumwamba, pali ponche ikaukondwela ubwino wake wene neema kutijela ife chipenyelele ndi finikizo la mtundu uli wonche. Ndi sichikadakalapo chakutontoza wantu Wa Kristo, kupunda ichi kuti wachitidwe kufwanana ndi Kristo, pa kuva chijizingile mafinikizo, masauko, ndi ntenda. Pakuti iye mwene wake sadakwela kwa kusekelela mpaka sanave mapwetekecho; iye sanaloa pa kukuzika kwake yapo akali sanatalamichidwa ya msalaba. Chimwechija zene zene njila yatu ya kutiikila mkusekela chikalile mmwemoje ndi kuva masaucho pano pamoji ndi Kristo; ndi komo latu lakuloa pa kulama chikalile mmwemoje ndi kufa pamoji ndi Kristo chikondwele; kuti tizyuke pa kufa, ndipo tikalongeze pamoji naye pa kulama chikalile mmwemoje. Ndipo chapano, ukalandile kudwala kwako uku kukukomela chimwechi, chijizingile, ndikuchisa, pa Jina la Mlungu, kukumbukila umo udajivumbulila pa nkope ya Mlungu pa Ubatizo wako. Ndipo pakuti pambuyo pa umoyo uu wa pano sikuwelengedwe kwa Wolamula wochita malinga uyo wonche sangasie kulamulidwa naye,

popanda kusanka ali yenche, ndikufuna kuti ujilinge umwene wako ndi umo ukalila chidya la Mlungu ndi chidya la wantu; mmwemo ukajichimikiza umwene wako ndi kujipacha mlandu umwene wako umo umalakwila, ukomane ndi lisungu pa janja la Atate watu wa Kumwamba chifuko cha Kristo, ndipo wosachimikizidwa ndi kutuluchidwa wakulakwa pa mlandu uja wa kuofya. Mmwemo sindikufotokozele mbua mbua za Mvano watu, upate kujiwa ngati uvomeladi, umo mKristo akadavomelela, pena ngati ukala wosavomela.

¶ *Pa malo yapa Wotumikila Mlungu ajichatiza mbua mbua za Mvano,*

Kodi umvomela Mlungu Atate Mwene mpavu zonche, Wopanga Kumwamba ndi jiko?

Ndi Yesu Kristo Mwana wake wobadwa yeka Ambuye watu? Ndi kuti adatengedwa mimba ndi Mzimu Woyera; wobadwa ndi Maryamu Virgin; ndi kuti adasauchidwa pa nyengo za Pontio Pilato, wotalamichidwa pa msalaba, wakufa, woikidwa pa manda; kuti adachika pa malo pa mizimu, ni sonincho siku la katatu adazyuka pa wakufa; kuti adakwela kumwamba, ndi akala panchi pa janja la kwene la Mlungu Atate mwene mpavu zonche; ndi kuchoka kumweko saajencho pomalizika vyaka, awalamule wakulama ndi wakufa?

Kodi umvomela Mzimu Woyela; Church Loyela ndi Katoliko; Kusanganizana kwa Woyela; Kulekeledwa zambi; Kuzyuka kwa tupi; ndi kulama kwa vyaka pambuyo pa kufa?

¶ *Wodwala ajiyanka.*

Yanko. Aya yonche ndivomela, wosakaikila.

¶ *Ndipo Wotumikila aiimyesela bwino kuona ngati alapa zene zene pa zambi zake, ndi ngati ailana ndi wantu wonche; kumchisa iye kuti alekelele ndi mtima wake*

wonche yawo wadamchwalicha; ndi ngati iye mwene wake adawachwalicha wina, kupempa kuti wamlekelele; sonincho yapo anampwetekecha mnjake kapena wosamchitila malinga, alipe chizazile umo sakozele. Ndipo ngati akala sadaikilatu umo chuma chake chikadagawidwila, ajininkidwa njelu pa nyengo iyo kuchita Chikalakala cha kugawu chuma chake, ndi kutulucha Mangawa yake, yayo adakongola, ndi yayo adakongolecha wena; kupunda kukwerukicha maganizo yakumchimikiza pa mtima wake, ndi kuti yawo sasunge pa kugawa chuma chake asapata mlandu chaje. Nampo wantu wakadakumbukichidwa kawili kawili kuyambiza kuti waike chuma wali nacho pa jiko lino chiiiwikile, yapo akala chisangalalile.

¶ *Mau yaya yafotokozedwa pamwamba yakoza kunenedwa pachogolo Wotumikila Mlungu sanaliyambe Pempelo lake, umo sakaonele kutometamo.*

¶ *Wotumikila Mlungu sakadasia kuchisa ndi likwale yawo walije mpavu mtupi yawo sakakoze kuchita chimwechi kukoma pakosi kwa wampawi.*

¶ *Pa malo yapa uyu alije mpavu mtupi okadapachidwa njelu kuvumbula zambi zake iye mwene, ngati akaona kuti bwalo la pa mtima wake lisauchidwa ndi mlandu wakulemelela. Ndi yapo akata kuvumbula chimwechi, Kasis ajimmasulila (akafunadi kwa kujichicha ndi kwa ntima wa mpumpu), kuchaticha mau yaya.*

Ambuyatu Yesu Kristo, uyo adasia bwalo pa Church lake, kumasula wonche wene zambi yawo walapa zene zene ndi wavomela pa iye, kwa lisungu lake lalikulu akumasule pa vochimwicha vako: Ndi kwa mpavu izo za bwalo izo ndinagwilizidwa, ndikumasula pa zambi zako zonche, Pa Jina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyela. Amen.

¶ *Ndipo Kasis ajinena Pempelo la chidule ili lichatalo.*

Tipempe.

Mlungu wa maganigani viwi, pa kuchuluka malisungu yako umachocha zambi za yawo wakulapa zene, mpaka wasazikumbukilancho; cheuka maso yanu ya lisungu pa uyu kapolo wanu, uyo afuniladi ndi mtima kuti asasungidwancho mlandu nampo kulekeledwa. Uchichite cha chapano, Atate wakukonda viwi, chili chonche icho chidaonangika ndi kunyengeza ndi usokolo wa diabolo, kapena ndi kufuna kwake mwene wake pa nyama ndi kutyala kwake; Umlindilile ukamwimiche uyo chiwalo chakudwala pa umoji wa Church; Muunguze umo akalila ndi mtima wabwino pa kulapa, Mlole misozi yake, Mpweche mapwetekecho yake, umo simukuonekele kumkomela viwi. Ndipo pakuti akulupilila chikulupilile pa lisungu lanu loka, msamwelengela zambi zake za kale, nampo mumtilile mpavu ndi Mzimu wanu wolumbidwa Mwawi wene; ndi yapo simkonde kumtenga kuchokela pa jiko lino, ukamlandile pa kukondwela kwako, kwa voyenela va Mwana wanu wokondedwa viwi, Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

¶ *Ndipo Wotumikila Mlungu ajinena Zabur ii.*

In te, Domine, speravi. Zabur lxxi.

Iwe, Ambuye, ndikutawila : nisatilidwa manyazi mmwemoje.

Pa kuchita malinga kwako univuule, ukanipule: unipendekele kutu lako, ukanipulumuche.

Ukale kwa ine chimwala cholama chakukalilapo, uko nimukeko chimukile : wataukila kunipulumucha; chifuko Iwe chimwala chakusongoka changa, ni linga langa.

Unipule, Mlungu wanga, pa janja la wakuipa : pa janja la uyo wopotocha ndi wosinikalila.

Chifuko iwe ncho ndikukumbatila, Ambuye Mlungu : kukulupilila kwanga, chiyambile ubwana wanga.

Ndachilikizidwa ndi iwe chiyambile pa mimba : Iwe umwene wanitulucha pa matumbo ya amaye ; sinikulumbe chilumbile.

Ndili ngati chidelu kwa wanyinji : nampo Iwe uko nitawilako kwene mpavu.

Pakamwa panga sipajale ndi malumbo yako, ndi kapambidwe kako usana wonche.

Usanitaya pa nyengo ya kukota : pa kulala nkongono zanga usanisia.

Chifuko woipila wanga wakuti ya ine : ni yawo wakuulindilila umoyo wanga wapangana malango,

Kuti, Mlungu wamsia : mlondeni, kamgwileni ; chifuko palije wakuvuula.

Mlungu usamuka kwa kutali kwa ine : Mlungu wanga, fulumiza kunitangatila,

Watilidwe manyazi wakalale wakuuchucha umoyo wanga : wavinikilidwa ndi kukojedwa ni vipongwe yawo wafunafuna voipa kwa ine.

Nampo ine sinijilindikize chijilindikizile, ndi sinionjezele pamwamba pa kulumba kwako konche.

Pakamwa panga sipawerenge kuchita malinga kwako, ndi upulumuchi kwako usana wonche : chifuko sindijiwa mawerengedwe yake.

Sinije ni vamwamuna va Ambuye Mlungu : sinikubukiche umo uchitila malinga, umo uchitila Iwe weka.

Mlungu, waniyaluza chiyambile ubwana wanga : ndi mpaka chapano udayeneza vopambana vako.

Yetu, ingakale nikakota, ni nikakala ni nyivi, Mlungu, usanisia : mpaka sinidayeneze janja lako kwa chibadwa chinjake, ni chimwamuna chako kwa ali yenche uyo saaje.

Kuchita malinga kwako ncho, Mlungu, kuli ponyamulidwa : Iwe wakuchita vavikulu, Mlungu, yani ngati Iwe ?

Akuzike Atate, ndi Mwana : ndi Mzimu Woyela ;

Umo kumakalila poyamba, chimwechi ndi chipano : ndi kwa vyaka vosata. Amen.

¶ *Kuonjezela ali.*

Mpulumuchi wa jiko, kwa Msalaba wanu ndi Mwazi wene ntengo mdatiombola, Mkatipulumuche ife, ndi mkatitangatile ife, tikupembezani kujichicha, Ambuye.

¶ *Ndipo Wotumikila Mlungu ajinena,*

Ambuye mwene mpavu zonche, uyo ali chilindo chene mpavu nditu kwa wonche yawo wakumkulupilila iye, uyo vintu vonche ivo vili Kumwamba, ndi pa jiko, ndi panchi pa jiko, vimwelamila ndi kumvela, akale chapano ndi kwa vyaka va chikalileje wakuombelela wako ; ndipo akujiwiche ndi akuvereche, kuti palije Jina linjake lapelekedwa kwa wana wa adam panchi pa Kumwamba, mkati mwa ilo ndi kwa ilo, ukoza kulandila kusangalala ndi kupulumuka, ikawe Jina la Ambuyatu Yesu Kristo loka. Amen.

¶ *Ndi pambuyo pake ajinena,*

Kwa lisungu lene neema la Mlungu ndi kwa kulindilila kwake tikuikizapo. Ambuye akuninke mwawi, akusunge, Ambuye ang'aliche nkope yake pamwamba pa iwe, akuchitile vakukondwecha. Ambuye anyakule nkope yako pa iwe, ndi akuninke mtendele, chapano ndi kwa vyaka va chikalileje. *Amen.*

Pempelo kwa mwana modwala.

Mlungu mwene mpavu zonche, ndi Atate mwene lisungu, ni kwanu koka machokelo ya kulama ndi ya nyifa ; Zuzumilani kuchokela Kumwamba ndi maso ya lisungu, tikupembezani kujichicha, kupenyela mwana uyo chapano ali mkugona pogonela pakudwalila. Mumjele, Ambuye, chipenyele ndi upulumuchi

wanu : mumvuule pa nyengo iyo yolangizidwa ndi mawene pa kupweteka kwake mtupi, ndi mpulumuche umoyo wake chifuko cha malisungu yanu ; Kuti, mkakonda kutanimpicha siku zake yapa pa jiko pano, akulamile imwe, ndi akale chopanganila cha kukuzika kwanu, pa kukupotelani ndi mvano, ndi pa kuchita vabwino, pa chibadwa chake : pena mmlandile kwanu pa malo yaja ya kulongeza Kumwamba, yapo maumoyo ya yawo wagonawo pa Ambuye Yesu wapata kukala pa kupuma chipumile ndi chimwemwe. Mtilengelele ichi, Ambuye, kwa chifuko cha malisungu yanu, pa mmweyuja Mwana wanu Ambuyatu Yesu Kristo, uyo alama ndi kukala mfumu chilamile pamoji ndi inu, ndi Mzimu Woyela, Mlungu mmoji, kwa vyaka va chikalileje. *Amen.*

Pempelo kwa muntu wodwala, yapo wosakoza kukulupilila kuti sasangalalencho.

Atate wa malisungu, ndi Mlungu wa kutontoza konche, moka mtitangatila pa nyengo ya kusowa ; Tikutawilani mtipokolele kumwimilila uyu kapolo wanu, chigonele yapa panchi pa janja lanu ndi kulenda kwakukulu pa tupi. Mmpenyele iye, Ambuye, ndi kukondwa ; ndi umo muntu wake wa kubwalo ali mkulala, mmtilile mpavu, tikupembezani, kupunda ni kupunda wosapuma ndi neema yako ndi Mzimu wako woyela pa muntu wa mkati. Mmninke kulapa kopanda kujilenga chaje kwa vosokelela vonche va pa kukala wa moyo mpaka chapano, ndi kumvomela Mwana wanu Yesu chivomelele ; zambi zake zichochedwe kwa lisungu lanu, ndi kulekeledwa kwake kukomedwe chizindikilo Kumwamba, pachogolo iye sadamukeko, ndi wosaonekancho pano. Tijiwa, Ambuye, kuti namba kantu kolepeledwa kwanu ; ndipo, mkafuna, simkoze ingakale chapano kumuuchancho, ndipo kumlengela kulongeza pakati pa ife vyaka vina ncho : Nampo pakuti mpaka kuoneka

kwake nyengo yake ya kupatukana tupi ndi nyama ili mkuwandikila, mpambe ndi mkamwikiletu, tikupembezani, kwa nyengo ya kufa, kuti pambuyo pa kuchoka pano pa mtendele, ndi pa kukukondwelani, umoyo wake ulandilidwe pa ufumu wanu wa chikalileje, kwa voyenela ndi kwa kuteteza kwake Yesu Kristo, Mwana wako yeka yeka, Ambuyatu ndi Mpulumuchi. *Amen.*

Pempelo lakupelekeza kwa muntu wodwala mkuchokaje.

Mlungu mwene mpavu zonche, kwa imwe mizimu ya wantu wakuchita malinga wochitidwa wotelanya nditu yalongeza, yapo wamasulidwa pochekelezedwa pa jiko pano, ife kujichicha tiikiza umoyo wa uyu kapolo wanu, mbale watu wokondedwa, pa manja yanu, ngati pa manja ya Wopanga wa mvano, ndi Mpulumuchi mwene mwene lisungu ; chikupembezeleni kujichichilatu, kuti ukale wene mtengo pa maso yanu. Chonde, muchuke, pa mwazi wa Mwana wa mbelele yuja wa shee, uyo adapedwa kuchocha zambi za mjiko : kuti vili vonche va chaje wavitengela pa kukala pakati pa jiko lino lene masauko ndi kuipa, pa kukumbila kwa nyama, kapena malindi ya Shetan, vichukidwe ndi kutimidwa, utuluchidwe wopanda ukazuzi ndi wa shee pachogolo panu. Ndi mtiyeluze ife pa kuchala pano, kupenya vintu ivi ndi vinancho vakutilangiza nyifa siku ndi siku, kuona umo makalidwe yatu yajityalila mpavu ndi yosajiwika ; ndipo kuziwelenga siku zatu, tisamala kutila mitima yatu kupata njelu zija za pa zoka ndi za Kumwamba, tikakalapo pano, izo sizikoze kutipelekeza ife pa kutela mpaka kulama kwa chikalileje mmwemoje, kwa ivo voyenela va Yesu Kristo Mwana wanu yeka yeka, Ambuyatu. *Amen.*

Pempelo kwa wantu yawo wakwezedwa mtima, pena ali ndi milandu pa bwalo la mitima yao.

Ambuye wolumbidwa Mwawi wene, Atate wa malisungu, ndi Mlungu wa kutontoza konche; Tikupembezani, mzuzumile ndi lisungu ndi kuvana ndi uyu kapolo wako wosauchidwa. Muli mkumlembela vowawa, ndi mmlovya mchokolo pa mpulupulu zake za kale; kupyecha mtima kwanu kumlemelela, ndi umoyo wake wajala ndi voipa: Nampo, Mlungu mwene lisungu, mwalemba Mau lanu lakuyela kutiyeluza, dala kuti ife, pa kujizinga ndi kujitontoza ndi Malembo yanu yoyera, tikadakala ndi chikulupi; Mmninke kujijiwicha bwino mwene wake, ndi Mau yanu ya kuombeleza ndi ya kulanga; kuti iye ingakale kutaya asataya chikulupi chake ali nacho pa imwe, angakale asakulupilila pena ncho ikawe pa imwe. Mmninke mpavu kuchucha mayeso yake yonche, mkamchiliche pa ntenda zake zonche. Usatyolelatu bango lodinyika, ingakale kutima msatima tonji lakutututuma uchi. Msachekeleza malisungu yanu ya kuolowa pa kupya mtima; nampo mmveke iye kuyangala ndi kusekelela, kuti vifupa vivine ivo mwavityola. Mpulumucheni pa chitente cha wakuipila, mkanyakule dangalila la nkope yanu pamwamba pa iye, ndi mninkeni mtendele, kwa voyenela ndi kuteteza kwake Yesu Kristo, Ambuyatu. *Amen.*

KUSANGANIZANA KWA WODWALA.

¶ *Pakuti wantu wonche wosatasima, wokamanika ndi voluswa vavinyinji chizilimukila, ni utenda, ni volenda, ndi chikalile wosajiwa chakanji sachoke pa umoyo uu wa pano; mmwemuno, dala kuti siku zonche waikidwiletu kufa, pali ponche Mlungu mwene mpavu zonche sakonde kuwatana, Wosungila siku zina zina (ni maka maka pa nyengo ya chipindupindu, kapena ya utenda wina wa kuyambukila lumbwe) kwa njeza sachise wantu wa Paroikia yao walandile kawili kawili Kusanganizana koyela pa tupi ni mwazi wa Mpulumuchi watu Kristo, yapo sikuchitidwe kumtumikila Mlungu pa bwalo pa Church; kuti pa kuchita chimwechi, wakale opanda ndande ya kumwaza mtima pa kusowa kumweko wakapenyeledwa ni Mlungu chizizimukila. Nampo ngati wodwala wosakoza kufika pa Church, afuna nampo kulandila Kusanganizana mnyumba mwake; ndipo sangachedwe kumumila Wosungila, ndi kufotokoza wangati wakalapo sasanganize naye, (yawo wajikala watatu kapena, ati maka wakachepekedwa viwi, wawili,) ndipo akakala ndi malo poilanapo pa nyumba ya uyo adwala, ndi vonche ivo sivifunidwe voikidwilatu, dala Wosungila amtumikile Mlungu ni ulemu, pamwepo ajichita Kusanganizana koyela, kuyamba ni Pempelo la chidule, Epistola, ndi Evangel, izo zichatazo.*

PEMPELO LA CHIDULE.

Mlungu mwene mpavu zonche, wa umoyo wosatela, Wakuwapanga wanu adam, muwalanga yawa muwakonda, muwatyapula yawa muwalola; Tikupembezani

kumlengela lisungu uyu kapolo wanu uyo janja lanu linamjela, ndi alenjele kujizinga pa utenda wake, ni kupata kusangalala ncho pa tupi lake, (ngati mkafuna chimwechi kwa neema yanu ;) ndi pali ponche mtima wake siuchoke pa tupi, utuluchidwe pachogolo panu popanda banga ; mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

EPISTOLA. *Heb.* xii. 5.

Mwana wanga, usapepula kulanga kwake Ambuye, usakomoka pakunyindilidwa naye. Pakuti uyo Ambuye amkonda, amlanga ; amtyapula mwana ali yenche uyo amlandila.

EVANGEL. *W. Yoh.* v. 24.

Zene, zene ndikunenelani, Uyo avela mau langa, ndi avomela pa uyo adanituma, ali ni kulama kosatela, wosaloa kutuluchidwa woipa pa milandu ; nampo wasamuka pa kufa kuloa pa umoyo.

¶ *Pambuyo Kasis ajiyenda mchogolo kwa mlingo wa chifa cha mau aya yalembedwa pamwamba kwa Kusanganizana koyela, kuyamba kwa mau aya* (Inu wakulapa kwa zene, *&c.*)

¶ *Pa nyengo ya kugawila Sakrament ii yoyela, Kasis ajilandila uti mwene wake, ni pambuyo ajiwagawila yawo wolangizidwa kusanganizana ni uyo wodwala, ni potela wodwala mwene wake.*

¶ *Nampo ngati muntu, pa kupunda kudwala, kapena pa kuchedwa kumfotokozela Wosungila, kapena pa kusowa wakulandila pamoji naye, kapena chintu china chakuchekeleza cha malinga, wosailandila Sakrament ya Tupi ni Mwazi wa Kristo, Wosungila ajimyeluza, kuti ngati alapa zene kwa zambi zake, wosakaikila kuti Kristo anamfela pa Msalaba, ni kuti ananwaza mwazi wake kumombola, ndi akakumbukila ndi njeza ni mtima vokoma vija alandila mmwemo, ndi akayamika ni*

mtima kwa ivi, ndimo akudya, akumwa Tupi ni Mwazi wa Mpulumuchi watu Kristo mpaka chipatilile kusangalalicha Umoyo wake, angakale wosalandila Sakrament ija pa kamwa pake.

¶ *Yapo wamjela wodwala, ndi kumchitila Kusanganizana Koyela pa nyengo imoji, ndipo Kasis, asazengeleka, ajidula chifa chija cha Kupenyela pa Zabur* [Pa Iwo, Ambuye, nakulupilila, *&c.*] *ndi ajimuka moongokela kwa Kusanganizana.*

¶ *Pa nyengo ya Chipindupindu, ni Kudwala, ndi mautenda ena ena yakuyambukila wantu, yapo palije wa Paroikia, angakale awo wokala pafupi, wapatikana kusanganizana ni wodwala mnyumba zao, kwa chifuko cha kuopa utenda ungawayambukile, akapempadi wodwala, Wotumikila Mlungu yeka akoza kusanganizana ndi iye.*